JW.ORG™
Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

Kodi Anthu Amaimba Bwanji M’chinenero Chamanja?

Kodi mumadziwa kuimba?

Kodi mungathe kuimba nyimbo nambala 41 yamutu wakuti “Lambirani Yehova Muli Achinyamata,” kuchokera m’buku lanyimbo lakuti *imbirani Yehova?* Pezani nyimbo imeneyi m’buku lanu la nyimbo kapena koperani mawu ake pa jw.org. (Pitani pamene alemba kuti MABUKU > MABUKU.) Mawu a m’nyimbo imeneyi akukukumbutsani kuti muzilemekeza makolo anu komanso muzimvera Yehova Mulungu.

Kodi mukudziwa mmene anthu ovutika kumva amaimbira?

Iwo amaimba m’chinenero chamanja. Taonerani vidiyo ya nyimbo yakuti “Lambirani Yehova Muli Achinyamata” yomwe yaimbidwa m’Chinenero Chamanja cha ku America pa jw.org. (Pitani pamene alemba kuti MABUKU > CHINENERO CHAMANJA. Onetsetsani kuti mwasankha Chinenero Chamanja cha ku America.) Onani ngati mungathe kuganizira kuti zizindikiro zina za manjazo zikuimira chiyani.

▶ **TAYESANI IZI:** Pemphani munthu mmodzi kuti asankhe vesi limene amalikonda kuchokera m’Malemba Achigiriki (Mateyu mpaka Chivumbulutso). Werengani lembali pamodzi ndipo kenako pemphani munthu wina kuti awerenge lembalo m’chinenero chamanja. Kenako onerani vidiyo yosonyeza mmene lembalo limawerengedwera m’Chinenero Chamanja cha ku America pa jw.org. (Pitani pamene alemba kuti MABUKU > CHINENERO CHAMANJA. Onetsetsani kuti mwasankha Chinenero Chamanja cha ku America.) Yesani kutsanzira pamene mukuonera vidiyoyo.

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania